

Bill Wiese:

Mphindi 23 mu Hade



Nkhani yotengedwa kuchokera mu CD, OSATI kuchokera mu bukhu lake. Ngati mufuna nkhanu yonse, gulani bukhu lake! Iyi inachokera mu msonkhano mu mzinda wa Kansas, KS wotchedwa “Mzinda wa Kansas kufikira America”. Nkhani iyi mu Hade inachitika pa 23 Novembala, 1998.

(Mau oyamba analankhulidwa ndi olingeza)

Miyezi ingapo yapitayo, Mike Bickle, amene ndimagwira naye ntchito ku International House of Prayer, anandifunsa kuti ndiphunzitse za Gahena. Pamene ndinali kuwerenga pa mutu umenewu ndinapatsidwa Tepi ndi mnzanga wotchedwa Steve Carpenter. Mu Tepi iyi munali uthenga womwe mutamve wa Bill Wiese ndi Mkazi wake Annette. Uthenga wake unasuntha moyo wanga. Ndipo unasintha za m'mene ndimakhalira ndi banja langa, amnzanga ndi anthu amene sindimawadziwa. Ndinasinthikiratu. Sindikuonjezera, kotero chonde musanganize kuti ndikuyankhula nthano chabe. Zasintha za m'mene ndimaonera za zaka zochepe zomwe ndatsala nazo pa dziko la pansi. Ndipemphero langa kuti Mulungu akapanga zomwezo ndi inu lero. Sindingasinjirire kufunikira kwa uthenga uwu. Bill ndi Mkhristu. Anapereka moyo wake kwa Khristu ali ndi zaka 16. Wamdziwa Ambuye kwa zaka 32. Anakakhala ku California mu 1976 ndipo wakhala zaka 10 pansi pa utumiki wa Abusa a Chuck Smith ku Costa Mesa, ku California. Bill ndi wa malonda, pamodzi ndi mkazi wake. Kwa zaka 15 zapitazo, Bill wakhala ali mu mpingo ndi mu utsogoleri nthawi zosiyana za ntchito yotchedwa Eagles Nest, pansi pa utsogoleri wa Dr. Gary Greenwald, ku California. Mbusa wa kumeneko ku Eagles Nest wotchedwa Mbusa Raul anabwera kwa Bill miyezi ingapo nati, “*Bill, Mulungu agwira ntchito ya chitsitsimutso. Ayambira ku Mzinda wa Kansas ndi kufalikira mu America. Akakutumiza iwe kumeneko ndipo upite*” Bill ndi Mkazi wake Annette anali asanakhalepo ku Mzinda wa Kansas moyo wawo wonse. Mmawa wake ndinamuyimbira Bill ndikuti, “*Kodi ungabwere ku Mzinda wa Kansas? Ndakhala ndikuonera Video yako ndiye ndikuganiza kuti uyenera kubwera.*” Ndikukhulupirira ali pano pa lamulo la Mulungu.

Mukamva za masomphenya a Gehena, koma koposa apo mukamva za masomphenya a chiyanjano cha Yesu Khristu ndi chikondi chimene Iye ali nacho padziko lonse lapansi. Bill anali ku Gahena. Sikuti anangokhala okaonerera, monga m'mene anthu ena akhala ndi masomphenya, koma anakamva kuwawa kwa Gahena kwa theka la ola popanda chiyembekezo chothawa. Bill ndi mkazi wake ndi wozipereka kwa Yesu Khristu, ndikuntchito ya Mulungu, ndi kuutsogoleri wa Mzimu Woyera. Mukamukondanso. Chonde alandire Bill ndi Annette Wiese.

(Bill Akuyankhula)

Ndichinthu cha ulemu kukhala pano. Ulendo wonse wakhala mdalitso kwa ife. Monga m'mene Hal wanena, tili mu bizibizi yogulitsa nyumba. Sitimapanga ntchitoyi kuti tikhale ndi moyo. Sitigwira pofuna ndalama. Timadziwa kuti Mulungu watiuza ife kuti tipite pa dziko lapansi ndikuliuza za chikondi chake komanso za

malo amene iye safuna chilengedwe chake chitapita. Ndichifukwa chake tiri pano, ndikaufupikitsa umboniwu ndikukhala wa chindunji.

Koma poyamba ndikufuna ndikhudze zinthu zingapo, mafunso amene angathe kukhala mmutu mwanu. Funso loyamba lomwe lingakhale mwa ine, ndikanakhala kuti ndimamvetsera, likanakhala kuti, “Mukudziwa bwanji kuti sanali maloto chabe omwe munali nawo? *Maloto oyipa?*” zinthu zingapo zoti mudziwe, poyamba, ndinachoka mnthupi langa. Ndinaliwona thupi langa pamene ndinali kubwerera, liri potero. Kotero ndikudziwa motsimikizika kuti zimachitika ndili kunja kwa thupi langa. Akhristu ena anati, “Oh Mkhristu sangachoke mnthupi lake.” Koma izi sizoonza, mu 2 Akorinto 12:2, pamene Paulo anatengedwa kupita kumwamba kwa chitatu, Iye anati, “*kaya mnthupi, kapena simnthupi sindidziwa.*” Ndipo ngati sanadziwe ndiye kuti ndizotheka. Ndipo anatinso mu vesi 1 kuti anali masomphenya, kotero ndikukhulupirira izi zili mu gulu la masomphenya.

Mu Yobu 7:14 akuti, “*inu mumandiopseza ndi maloto ndi masomphenya.*” Tsono izi ndi zimene Ambuye anachita, kundiopseza ndi masomphenya. Komanso pochoka mu izi zinanditengera chaka kuti ndikhadzikike, ndikukhalanso ngati munthu. Ndinali odzala ndi mantha kotero kuti zinasintha maonedwe anga za m’mene tikuyenera kuchitira umboni za zimene Mulungu watipulumutsako ife.

Ndimufunse mkazi wanga kuti abwere kwa ka mpindi ndipo agawane nanu zomwe zinachitika pamene anadnipeza pa chipinda chochezera, chifukwa sindingakumbukire gawo limenelo. Kotero ndikufuna iye agawane nanu mau pang’ono. Zikomo.

(Mkazi wa Bill kuyankhula)

Inali 3:23 ku mmawa pamene ndinadzuka. Nditayang’na ndinaona kuti Bill sanali pafupi nane, ndipo ndinamva kukuwa kuchokera ku chipinda chathu chochezera. Ndinathambgira kumeneko. Ndinampeza mwamuna wanga asali m’mene ndimamudziwira. Ngati wina amamudziwa Bill, ndiwofatsa komanso wozigwira. Simunthu yemwe amangosangalala wamba kapena kutengeka-tengaka, pokhapokha ndi Mulungu. Komabe, ndinamuona wamantha, atagwira mutu wake akulira mokweza. Anali munyengo yoopsa pa chipinda chathu chochezera. Sindinadziwe choti ndingachite. Ndimaganiza kuti mwina akuyamba matenda a mtima. Ndinangoyamba kupemphera ndipo anakuwa kuti, “*Upemphere kuti Ambuye achotse izi mmaganizo mwanga! Ambuye ananditengera ku Gehena. Ndikumva ngati kuti thupi langa likufa, sindingathe kupirira izi.*” Kotero ndinapitiriza kumupempherera, ndipo pomaliza mphindi khumi kapena khumi ndi ziwiri anayamba kukhadzikika. Anali munyengo yamantha, monga wina yemwe anapita kunkhondo ya Vietnam kapena anali pangosi ya galimoto. Sizinali ngati munthu woti wangokhala ndi maloto oyipa ndipo wadzukapo. Ndiye ndimangofuna kuchitira umboni za izi.

(Bill kuyankhulapo)

Ndine wodalitsika ndi mkazi wabwino. Ndine wothokoza kwmbiri kwa Mulungu. Ndakhala pa banja kwa zaka zinayi ndipo ndamudziwa kwa zaka zisanu ndi chimodzi, ndipo zakhala zaka zanga zabwino kwambiri za moyo wanga, ndiyenera kunena, Ambuye alemelezeke.

Ndimafuna nditadziwa ngati panali munthu wina M’Baibulo yemwe anakhalapo ndi mpata wopita ku Gahena. Kotero ndinayamba kufufuza. Ndimamvetsera kwa Chuck Missler kwambiri. Ndi Mphunzitsi wa Baibulo yemwe akuphunzitsa mafuko ambiri ndipo anati Yona anakumana nayo Gehena. Mu Yona 2:2 akuti, “**Mu Gehena analira.**” Ndipo Yona 2:6 akuti, “**Mipilingizo ya dziko inanditsekereza kosatha, koma munandikwezera moyo wanga kuuchotsa kuchiongeko.**” Choncho panali munthu wina m’Baibulo yemwe anakumanapo ndi Gahena, Yona.

Ndimafunanso kupeza, chifukwa ndinakuzidwa masiku oyamba a Calvary Chapel, woti zokumana nazo zili zonse zomwe munthu wakumana nazo zizikhala kuti zilipo M’mau a Mulungu. Kotero ndinadziwa kuti ngati zomwe ndakumana nazo ndi zoonza, ziyenera kuti zilipo m’mau. Ndiye ndinayamba kufufuza ndipo ndinapeza malemba okwa 400 omwe amanena zomwe ndinaona, kumva, ndikukumana nazo ku Gahena. Zili kale m’baibulo, choncho zomwe ndikukuzani zilipo kale m’menemo. Nditchulako ena mwa mavesiwa pamene tikupitirira. Sindingatchule onse 400, koma ena a iwo. Ndinapezanso kuti panali anthu ena 14 omwe

anakumana napo ndi gawo la Gahean. Ambiri a iwo anali otsala pang'ono kufa, anthu omwe amafa mchipatala ndipo anauka.

Choncho kukamba mwa nsanga: Mkazi wanga ndi ine tinali kumapemhero a usiku a la Mulungu amene timakhala nawo pamodzi ndi azibusa athu. Ndipo tinapita kunyumba monga usiku wina uli wonse ndikukagona. Cha m'ma 3:00 ndinatengedwa. Sindinadziwe m'mene ndinatulukira mpaka pamene ndinabwerera. Ndipo Ambuye anafotokoza. Koma ndinaponyedwa chipinda cha ndende, monga ndende ina ili yonse, yokhala ndi makoma okandika kandika ndi zitsulo pakhomo. Sindinadziwe komwe ndinali. Chomwe ndimadziwa ndichoti munali mutentha kwambiri, kutentha koopsa. Kutentha koti kunali kovuta kukhulupirira, zoti ndinali ndi moyo. Ndimamva ngati kuti ndisungunuka ndi kutenthaku, koma ndinali ndi moyobe. Kunali kuwala mchipindamo kwa kanthawi, ndipo ndikukhulupirira kuti kupezeka kwa Ambuye kunalipo kuti ndithe kuona zinthuzo bwino bwino, koma munali mdima patangotha mphindi imodzi.

Mu Yesaya 24:22 akuti: “Ndipo iwo adzasonkhanitsidwa pamodzi, monga ndende zimasonkhanitsidwa m'dzenje, ndi kutsekeredwa m'kaidi....”

Miyambo 7:27 “Nyumba yache ndiyo njira ya kumanda, yotsikira ku zipinda za imfa’.

Mau okuti “dzenje” akutanthauza zipinda. Kotero kuti gawo la gahena linali zipinda za ndende, mayenje amoto ndi malo akulu a moto, kotero kuti ndinali mu chipinda cha ndende pa nthawi imeneyi.

Komanso pa Yona 2:6, “Mipilingizo ya dziko inanditsekeriza kosatha, koma munandikwezera moyo wanga kuuchotsa kuchionongeko ...”

Ndi Yobu 17:16 “Chidzatsikira kumipiringizo ya kumanda....”

Ndiye zonse zomwe ndinaona zinali m'Mau. Miyala ikunenedwa mu Yesaya 14:19

Ndinazipeza muchipindachi, ndipo zilombo zinayi zinali ndi ine mchipindamo. Sindinadziwe kuti zinali ziwanda pa nthawiyo, chifukwa ndinapita ngati munthu wosapululumutsidwa. Mulungu anazichotsa m'mutu mwanga zoti ndinali mkhristu. Sindinamvetse chifukwa chiyani, koma anandifotokozera pamene ndimabwerera. Zilombozi, sindinadziwe kuti zinali ziwanda, koma zinali zoopsa. Zinali mafiti apakati pa 12 ndi 13 kutalika, china muchiona mu video. Mmodzi wa anthu omwe akupereka umboni wawo, anaona chiwanda chomwecho chomwe ndinaona. Kotero mukaona kuti chimaoneka motani. Muli chithunzi chabwino mu video mmene mkulu wina anatengedwera ku Gehena. Ndi umboni wa Kenneth Hagin.

Chinali chamamba. Chinali ndi mamba thupi lake lonse, zibwano zikulu zikulu za mano akulu, ndi zikhadabo zotuluka kunjira, ndi maso olova mkati. Zinali zoopsa. China sichinaoneke ngati ngati ichinso, koma chinali ndi zinthu zokhala ngati malezala thupi lonse ndi nkono umodzi wautali ndi mapazi osakhala mchimake. Chili chonse chinali chopotoka ndi chosokonekera, chosalongosoka, mkono umodzi wautali ndi wina waufupi ndi zilombo zooneka moopsa kwambiri.

Ndipo zimanyoza Mulungu. Nthawi yonse zimatemberera Mulungu. Ndinadabwa, “Chifukwa chiyani akutemberera Mulungu?” Chifukwa chiyani akudana ndi Mulungu kwambiri?” Ndipo zinandiyang'ana kwa ine, ndipo ndinamva mkwiyo womwewo pa Mulungu, mkwiyo umwe zinali nawo pa ine, ndipo ndinaganiza: “Chifukwa chiyani zikundida? Sindinachite kali konse kwa izo.” Koma zinandida ndi mkwiyo womwe sindinauneponso pa dziko lapansi; woposa umene munthu angakhale nawo. Zinadida kwambiri, ndipo ndinadziwa kuti zinatimizidwa kuti zindizunze ine.

Panali zinthu zomwe ndinene, zomwe sindikudziwa m'mene ndinadzidziwira. Ku Gahena umadzindikira bwino kwambiri, umakhala watcheru koposa m'mene matupi athu aliri. Ndimadziwa zakutalika kwa malo, ndimadziwa za nthawi, ndi zina zambiri, koposa m'mene umadziwira ukakhala pano. Ndinadziwa kuti zinatimizidwa kuti zindizunje ine mpaka kale kale.

Ndinali nditagona nchipindamo ndipo ndinalibe mphamvu mnthupi mwanga. Ndinadabwa, “Chifukwa chiyani ndikulemphera kusuntha, chavuta ndi chiyani ndi ine?” ndinangodziwa kuti ndilibe mphamvu, ndipo ndinali opanda mphamvu. Chiwanda chimodzi chinangondigwira ndikundizutsa, ndikundiponyera kukhoma ngati galasi. Anangonditenga ngati galasi. Umo ndimene ndimapepukira, kapena mmene analiliri ndi

mphamvu. Ndikundiponyera kukhoma, ndipo fupa liri lonse mthupi mwanga linathyoka. Ndipo ndinamva kuwawa! Ndinangoyamba kugona pansa, kulira kufuna kuchitiridwa chifundo, koma zilombo izi zilibe chifundo chiri chonse, opanda chifundo.

Chimodzi chinadninyamula, ndipo chinacho ndi zala za malezala, chinangondi leza leza. Amangudula minofu yanga ndipo analibe kusamala za thupi lomwe Mulungu analilenga moopsa ndi mwamtengo wapatali. Chinali ndi mkwiyo wambiri pa ine; ndinadabwa, “*Chifukwa chiyani ndili ndi moyo, chifukwa chiyani ndikukhala mu izi? sindikumvetsa chifukwa chiyani sindinafe.*” Thupi langa linangokhala lolezeka lezeka. Ndipo panalibe magari, minofu yokha ikulendewera, chifukwa moyo uli mmwazi, ndipo kulibe moyo ku Gahena. Ndiponso kulibe madzi ku Gahena.

Mu Yesays 14:9-10 akuti:

Kunsi kwa kugwedezeke, chifukwa cha iwe, kukuchingamira podza pako; kuutsira iwe mizimu, ngakhale onse akuru akuru a dziko lapansi; kukweza kuchokera m’ mipando yawo mafumu onse a amitundu. Onse adzabvomera, nadzati kwa iwe, Kodi iwe wakhalanso wopanda mphamvu ngati ife? Kodi iwe wafanana nafe?

Masalmo 88:4

Anandiwerenga pamodzi nawo otsikira kudzenje; ndakhala ngati munthu wopanda mphamvu:

Ndipo tikudziwa kuti Satana ali ndi mphamvu, m’baibulo munali munthu waziwanda yemwe amathawa thawa m’ manda, ndipo akuti:

Marko 5:1-4

Ndipo anafika tsidya lina la nyanja, ku dziko la Agerasa. Ndipo pamene adatuluka mungalawa, pomwepo anakomana naye munthu wa mzimu wonyansa, amene anayesa nyumba yache kumanda; ndipo palibe munthu anakhoza kummanganso, inde ngakhale ndi unyolo; pakuti adafomangidwa kawiri kawiri ndi matangadza ndi maunyolo, naduladula matanagza; ndipo palibe munthu anli ndi mphamvu yakumfuya.

Samatha kumumanga; amadula maunyolo kukhala zidutswa zidutswa. Uyu anali munthu chabe wokhala ndi mphamvu za ziwanda. Ndinamvetsetsa kuti ziwanda izi zinali ndi mphamvu zoposa ka 1000 mphamvu za munthu. Kotero kuti ngakhale ndikanakhala ndi mphamvu za umunthu, sindikanatha kulimbana nazo. Ndimasoweka chifundo chawo, chomwe izonso zinalibe chifundo chiri chonse. Ziwanda ndi zimene zimayendetsa moyo wanu ku Gahena.

Fungo la ziwandazi ndi fungo la Gehena ndi losaneneka; sindingathenso kulifotokoza kwa inu. Kuli fungo la minofu ya kupsya ndi safuli. Fungo la ziwanda linali ngati suweji yophulika, nyama yowola, mazira oipa, mkaka wowola ndi kena kali konse komwe mungathe kukaganiza. Mutenge fungo ngati limeneli mulichulukitse ka 1000 ndikuliika mphuno mwanu. Ndipo mulipume. Linali loledzeretsa, loti lingathe kukupha, mutakhala kuti muli nthupi mutha kufa, ndi ndinadabwa, “*Chifukwa chiyani ndikukhala ndi moyo ndi fungo limeneli, ndi loipitsitsa?*” Koma siumafa umayenera kulipirira.

Zamwano zomwe amanena, potemberera Mulungu zalembedwa mu Ezekeili 22:26 “**Ndanyozedwa pakati pawo**”

Ansebe ache achitira choipa chilamulo changa, nadetsa zopatulika zanga, sasiyanitsa pakati pa zopatulika ndi zosapatulika, ndipo sazindikiritsa anthu pakati pa zodetsa ndi zoyera, nabisira masabata anga maso awo.

Kunyoza, kuyankhula kwa chipongwe.

Kuzunza komwe amachita kwa ine kunalembedwa mu Deuteronomo 32:22-24.

“Pakuti wayaka moto mu mkwiyo wanga, utentha dziko lapansi ndi zipatso zache. Nuyatsa maziko a mapiri. Ndidzawaunjikira zoipa; Ndidzawathera mibvi yanga. Adzaonda nayo njala. Adzanyekeka ndi makala a moto, chinonongeko chowawa; Ndipo ndidzawatumizira mano a zirombo, Ndi ululu wa zokwawa m’pdumbi.

Kotero kuli mano a zilombo pa iwe.

2 Samueli 22:6 imanena kuti:

Zingwe za kumanda zinandizingira; Misampha ya imfa inandifikira ine.

Ndipo ku Mika 3:2 kuli mavesi osangalatsa kumene Afilisti, amene amadana ndi a Israeli amati:

Inu amene mudana nacho chokoma ndi kukondana nacho choipa; inu akumyula khungu lao pathupi pawo, ndi mnofu wawo pa mafupa awo;

Izi ndi zimene anachita kwa anthu a chiyuda. Izi zinali za kuthupi, koma ganizo limeneli analitenga kuti? Izi zimachokera ke Gahena. Izi ndi zimene ziwanda zimachita, ndi chifundo? Kumwamba kuli chifundo chokha chokha. Chifundo chimachokera kwa Mulungu, ndipo satana alibe chidziwitso cha mtundu wina uliwonse wa chifundo, amatsutsana nazo kwathuthu. Masalmo 36:5

“Yehova, m’mwamba muli chifundo chanu; Choonadi chanu chifikira kuthambo.”

Kulibe ku Gahena. Ndipo mu Masalmo 74:20 akuti:

Samalira chipanganochi; pakuti malo amdima a m’dziko adzala ndi zokhalamo chiwawa.

Ndi malo a nkhanza, omvetsa chisoni, oopsa amene muyenera kuwapirira. Umayenera kupirira zinthu zonsezi.

Mulungu anapanga kuti munthu akhale cholengedwa chapamwamba, ndipo ziwanda zonsezi ndi mtundu wa chilengedwe wotsika. Monga anthu timagwira ntchito kuti tipite patsogolo m’moyo, timazitukula tokha, timaphunzira. Koma ku Gahena, moyo wanu umayendetsedwa ndi ziwanda. Zilombo izi sizimaganiza, ndi zaumbuli. Zimene izo zimadziwa ndi mkwiyo pa Mulungu, mkwiyo pa inu ndi kuzunza. Ndipo zimayendetsa moyo wanu, ndipo simungathe kuchita china chili chonse pa izi.

Pali mavesi amene amakamba za kuchepetsedwa komwe muyenera kukupirira. “Chinthu ichi chialmulira moyo wanga, sindingathe kuchiletsa.” Ku Yesaya 5:14-15

“Ndipo manda akuza chilako lako chache natsekula kukamwa kwache kosayeseke; ndi ulemerero wao, ndi unyinjira wao, ndi phokoso lao, ndi iye amene akondwerera mwa iwo atsikira mommo. Munthu wonozeka waweramitsidwa, ndi munthu wochuka watsitsidwa; ndi maso a wodzikweza atsitsidwa;

Yesaya 57:9-16

“Ndipo unanka kwa mfumu, utadzola mafuta ndi kuchulukitsa zonukhira zako; ndipo unatumiza atumwi ako kutari; ndipo wadzichepetsa wekha kufikira kungsi kwa manda. Unatopa ndi njira yako yaitali; koma sunanene, Palibe chiyembekezo ; iwe wapeza moyo wa dzanja lako; chifukwa chache sunalefuka. Ndipo ndi yani amene wamuopa ndi kuchita naye mantha, kuti wanama, osakumbukira Ine, kapena sindinakhala chete nthawi yambiri, ndipo iwe sundiopa Ine konse? Ndidzaonetsa chilungamo chako ndi ntchito zako sudzpidula nazo. Pamene pakupfuula iwe akupulumutse amene unawasonkhanitsa; koma mphepo idzawatenga, mpweya udzawachotsa onse; koma iye amene anandikhulupirira Ine adzakhala ndi dziko, nadzakhala nacho cholowa m’phiri langa lopatulika. Ndipo adzanena, Undani, undani, konzani njira,

chotsani chokhumudwitsa m'njira mwa anthu anga. Pakuti atero Iye amene ali wantari wotukulidwa, amene akhala mwachikhalire, amene dzina lache ndiye Woyera, Ndakhala m'malo Atari ndi oyera, pamodzi ndi yense amene ali wa mzimu wosweka ndi wodzichepetsa, kutsitsimutsa mtima wa osweka. Pakuti sindidzakutsutsana ku nthawi zonse, sindidzakwiya masiku onse; pakuti mzimu udzalefuka pamaso pa Ine, ndi miyoyo imene ndinailenga.”

Ezekieli 32:24

Elamu ali komwe ndi gulu lache lonse lozinga manda ache; ophedwa onsewo, adagwa ndi lupanga; amene anatsikira osadulidwa kungsi kwache kwa dziko, amene anaopsetsa m'dziko la amoyo, nasenza manyazi zwo, pamodzi ndi iwo akutsikira kudzenje.

Choncho zimakhala zopitirira machitidwe ake. Chinali chinthu choopsa, kuyendetsedwa moyo wako ndi zilombo ngati izi, zomwe zilibe chifundo pa iwe mwa mtundu uliwonse.

(Mdimu ndi kulira ku Gahena)

Ndinali nditagona pansu mchipinda ndipo munada kwambiri. Ndikutanthauza za mdima womwe sindinamvepo chikhalire. Ine ndalowapo mapanga, pansu pa migodi ku Arizona. Kunali mdima oti simungaufanizire ndi chinthu chiri chonse. Ndinayetsetsa kukwawa kuti ndituluke, ndinatha kukwawa ndipo zinandilola. Ndikukumbukira pamene panali khomo kotero ndinakwawira kumene linali ndipo kenaka ndinatuluka mu chipinda chija. Ndinayang'ana mbali iyi, mdima wokha wokha, ndipo ndinamva kukuwa, anthu ochuluka akulira malo amenewa. Ndinadziwa kuti anali mabiliyoni, ndipo kunali kokweza. Ngati munamvapo munthu akukuwa, zinali zosasangalatsa. Inu mutamva anthu mabiliyoni akukuwa, simungathe kulingalira mmene zingamvekere maganizo anu. Simungathe kupirira. Mumagwira makutu anu chifukwa zimakhala zokwera komanso zopweteka mmakutu. Simungathe kuthawa kukuwa kwake.

Ndipo mantha amene amakugwirani inu ndi osaneneka. Chili chonse chimakhala chogwidwa ndi mantha. Kulibe kupezeka kwa Mulungu malo amenewa, ndiye mumayenera kuwapirira mantha ndi kuzunzika ndi mdima. Simungathe kuona kali konse. Simungathenso kuona chimene chikubwera kutsogolo kwanu. Mau amanena za mdima umenewu pa Masalmo 88:6

Mundandiika kungsi kwa dzenje, kuli mdima, kozama.

Chibvumbulutso 16:10

Ndipo wachisanu anatsanulira mbale yache pa mpando wachifumu wa chirombo; ndipo ufumu wache unadetsedwa; ndipo anatafuna malilime awo ndi kuwawa kwache.

Yuda 1:13

Mafunde oopsy a nyanja, akuwinduka thobvu la manyazi a iwo okha; nyenyezi zosokera, zimene mdima wakuda bii udazisungikira kosatha.

Ndipo kuli mdima woti umachita kuumva, monga analembera pa Ekisodo 10:21

Ndipo Yehova anati kwa Mose, Tambasulira dzanja lako kuthambo, ndipo padzakhala mdima wokhudzika.”

Mungathe kuukhuza mdima.

(Mantha a ku Gahena)

Mantha, amene ndinali nawo anali amphamvu. Amakugwira iwe. Ngati munawonerapo kanema wochititsa mantha, amene mantha amakugwirani, ngati mungathe kutenga mantha amenewa ndikuwachulukitsa ndi

kachikwi chimodzi, ndikukhala nawo, umu ndi m'mene mumakhalira nthawi yonse! Ndipo ndikudziwa china chake chokhudzana ndi mantha. Pamene ndinali wang'ono, ndimakonda kukasambira. Pamene ndinali wan'gono kwambiri tinali ku Coco Florida kukasambira ndipo panali chigulu cha dzinsomba zotchedwa ma Shark zimabwera komwe kunali ine. Ndipo chinsomba chotalika mafiti 9 chinabwera ndikuluma theka la thabwa lomwe ine ndimagwiritsa ntchito posambira. Inandigwira ine pa mwendo ndi kundigwetsa pansu. Ndiye mwendo wanga unali mkamwa mwa Shark. Sindinali Mkhristu pamenepo; ndinali ndisanapulumsidwe. Ndipo mwadzidzidzi, inandisiya. Ndikudziwa Mulungu anatsegula kukamwa kwa Chinsombacho. Koma kwa ka ntahwi, mantha amene amabwera mwa iwe amakhala akulu. Ngati wina anawonapo ZIBWANO, mantha ndi chabe koposa kulowa mu zibwanozo. Mantha ake anali oopsa. Mkulu yemwe anali pafupi ndi ine Nsombayo inachotseratu mwendo wake. Anamukokera kumtunda, ndimagazi pena pali ponse. Amalira mokuwa ndipo analibe mwendo. Kotero ndikumvetsetsa mantha, koma mantha amenewo ndi chabe, ndipo ndi chabe kuyerekeza ndi mantha omwe ndinamva ku Hade, simungafanizirensa ayi. Ndikukhulupirira kuti mantha amene ndinali nawo pamene ndinakumana ndi chinsomba ndi a modzi mwa mantha tingathe kukhala nawo padziko lapansi.

Choncho izi ndi zina mwa zinthu zimene zomwe timayenera kuzipirira ku Gahena. Mu Yesaya 24:17 akuti:

Mantha ndi dzenje ndi msampha ziri pa iwe, wokhala m'dziko. Ndipo padzali, kuti iye amene athawa mbiri yoopsya, adzagwa m'dzenje; ndi iye amene aturuka m'kati mwa dzenje, adzakodwa mumsampha, pakuti mazenera a kuthambo atsegulidwa, ndi mazilo agwedezeka."

Ted Koppel, pamene amapanga filimu yake ya "Night Line" chaka chimodzi ndi theka chapitacho, anakafika zina mwa ndende zathu mdziko lathu ndipo anagona usiku umodzi ku ndendeko. Sanathe kukhulupirira phokoso lomwe linali kumeneko, kotero kuti sakantha kugona, aliyense kumangukuwa. Ananena pa wailesi ya kanema kuti anali odabwa za mmene anthu angamakhalire kumangukuwa ndikupanga phokoso usiku wonse. Choncho ngakhalsenso mdende zathu pa dziko lapansi, anthu akulira, ndi kukuwa, nanga kulibwanji ku Gahena. Mu Yobu 18:14 akuti njira ya munthu woyipa, munthu amene amakana Ambuye....

Adzadulidwa kuhema kwache kumene anakhulupirira; zadzatengedwa kunka naye kwa mfumu ya zoopsa.

Satana ndi mfumu ya zinthu zoopsa.

(Osowa chiyembekezo ku Gahena)

Ndinali tsopano kunja kwa chipinda ndipo ndinayang'ana ndipo pamene ndinayang'ana mbali ina kunali Malawi a moto, kutalika kwa malo ake kofanana ndi mtunda wokwana mamailosi khumi. Ndi dzenje la moto, lalitali pafupi fupi mamailosi atatu, linali ndi Malawi a moto omwe amatha kuwalitsa malowo zomwe zimapangitsa kuonetsa malo a Gahena pang'ono.

Mdima unali wochuluka woti umangomeza kuwala kuli konse. Koma kunalipo kongokwanira kuonako pang'ono. Kunali kwa psyuu ndipo kopanda chili chonse! Ndikutanthauza ngakhale tsamba limodzi lobiriwira, kopanda china chili chonse cha moyo, koma mwala, okuda ndi mtambo wakuda. Malawi anali aatali, kotero ndimawaona. Panali vesi pa Deuteronomo 29:23

Ndi kuti lidapsa dziko lonse ndi sulfure, ndi mchere, kuti sadzalamo, kapena siliphuka kanthu kapena sumerapo msipu monga kupasula kwache.ndi ukzli wache.

Kunalibe moyo wantundu uliwonse ku Gahena. Chinali chodabwitsa kukhala mdziko lomwe munalibe moyo. Kuno timasangalala ndi mitengo ndi mpweya wabwino, koma uko ndi koferatu.

(kutemtha)

Kutemtha kunali kochuluka, mungathe kukufotokoza. Deuteronomo 32:24 amati;

Adzaonda nayo njala. Adzanyekeka ndi makala amoto, chionongeko chowawa; ndipo ndidzawatumizira mano a zilombo. Ndi ululu wa zokwawa m'pfumbi.”

Yuda 1:7

Monga Sodomu ndi Gomorra, ndi midzi yakuizungulira, potsatana nayoyo, idzapereka kudama, ndi kutsata zilako lako za chilendo, iikidwa chitsanzo, pakuchitidwa chilango cha moto wosatha.

Masalmo 11:6

Adzagwetsa pwata pwata misampha pa oipa; moto ndi miyala yasalfure, ndi ,phepo yoopsa zidzawagawikira m'chikho chawo.”

Izi ndi zomwe zikuchitika ku Gahena, ndikotentha. Zinthu zonsezi zikuyenera kukupha iwe, koma siumafa! Ukuyenera kumangozimva ndi kuzipirira. Ndimafuna mtendere wa mmaganizo, kuti nditalikane ndi kukuwa ndi kutuluka kumaloko. Zili ngati ukamafuna kupita kunyumba usiku utakhala ndi tsiku losasangalatsa, umangofuna mtendere wa maganizo. Koma uku umapirira kukuwa ndi kuzunzika. Ndipo siumathawa. Mu Yesaya 57:21 amanena kuti:

Palibe mtendere, ati Mulungu wanga, kwa oipa.”

Umakhalanso wa maliseche ku Gahena. Ndi chinthu chinanso chomwe umayenera kupirira. Manyazi! Mu Ezekieli 32:24 amanena za manyazi a kudzenje.

Elamu ali komwe ndi gulu lache lonse lozinga manda ache; ophedwa onsewo, adagwa ndi lupanga amene anatsikira kudzenje. Pakati pa ophedwa anamuikira kama, iye ndi aunyinji ache onse, manda ache amzinga, onsewo osadulidwa, ophedwa ndi lupanga, pakuti anaopsetsa m'dziko la amoyo, nasenza manyazi awo, pamodzi ndi iwo akutsikira kudzenje, aikidwa pakati anaopsetsa m'dziko la amoyo.

Ndipo pa Yobu 26:6

Kumanda kuli padagu pamaso pache, ndi kuchionongeko kusowa chophimbako.

Kutanthauza kuti Mulungu amaona mu Gahena, kotero ndikuoneka kwa Iye. Komanso umakhala wamaliseche ku Gahena, chinthu china chimene umayenera kudutsamo.

(kuuma)

kulibe madzi ku Gahena, kulibiretu, kopanda madzi. Kulibe mpweya opangitsa madzi ndiye kulibe madzi a mtundu uliwonse. Ndikouuma, umafufuna kadontho ka madzi, ngakhale kamodzi. Monga mmene malemba amanena ku Luka 16:23-24,

Ndipo adzanena ndi inu, Taonani ilo! Taonani ilo ! musachoka kapena kuwatsata; pakuti monga mphezi ing'anipa, kuchokera kwina pansu pa thambo, kotero adzakhala Mwana wa munthu m'tsiku lache.

Abrahamu anati, “Mwana kumbuka”, ndipo anapitiriza kukamba za a zichimwene ake. Amangofuna iye aike chala chake m'madzi ndikudonthezera, dontho limodzi. Izi zikanakhala zabwino, dontho limodzi, koma kulibe, kupeza kadotho ka madzi. Ndikovuta kulingalira za m'mene mkamwa mwanu mungakhalire mouuma. Ngati mungaganize mukuchita mpikisano mchigwa cha imfa mutaika thonje mkamwa mwanu ndipo likhale momwemo kwa masiku, ndiye zizingokhala choncho, kouma, mukhala ofunitsitsa kadontho kamadzi.

Chinthu china chimene tinaona ndichoti panali phompho pakati pawo, ku Gahena; pakati pa Paradizo ndi Hade. Ndipo munthu wolemera anaona Abrahamu ali kutali. Mnthupi akanamuzindikira Lazaro ndi Abrahamu bwanji? Poyamba anali asanakumanepo ndi Abrahamu ndipo kumuona munthu ali patali,

siungathe kumudziwa kuti iye ndi ndani. Koma kuli zinthu zina zomwe umangozidziwa ku Gahena. Umamvetsetsa, monga mmene ndimanenera, kuya, kotalika ndi zina zotero.

Kenaka chimodzi mwa ziwanda zija chinandigwira ine, ndikundikokera kundibwezera mchipinda muja ndikuyamba kundizunzanso, zomwe ndimadana nazo kuzikamba, chifukwa sindimafuna kukhala ngati ndikudzikhala zowawa zomwe ndinakumana nazo. Anayamba kupwanya mutu wanga. Chiwanda china chinandigwira kufuna kupwanya mutu wanga. Ndimakuwa ndikuyesera kupempha chifundo, koma kunalibe chifundo! Pa nthawi imeneyi aliyense anagwira dzanja ndi mwendo ndipo anatsala pang'ono kundikhadzulirana. Ndinaganiza, “*Sindingathe kuzipirira izi, sindingathe kuzipirira izi!*”

(Pafupi ndi Dzenje)

Ndipo mwadzidzidzi china chake chinandigwira ndikundikokera kunja kwa chipindacho. Ndikudziwa anali Ambuye, koma nthawi imeneyo sindinadziwe zimenezo. Ndinali kumeneko monga munthu wosapulumsidwa, kotero sindinadziwe zinthu zimenezi. Ndinangopita kumeneko ngati kuti sindinalandirepo Ambuye. Ndinayikidwa pafupi ndi moto womwe ndinauona. Ndimaima pafupi ndi dzenje. Ndinali pansu pa gomolera, monga dzenje lalikulu, ndi njira yotulukira mmwamba. Mbali mwa moto ndimatha kuona Malawi, otha kuona matupi, anthu ali m'moto akukuwa, kukuwira chifundo, akupsya! Ndipo ndinadziwa sindimafuna kupita m'menemo. Ululu omwe ndimaumva unali okwanira, koma kutentha kochokera kumalawi ndinadziwa kunali kopitirira muyezo. Anthu awa amapempha kuti atuluke.

Kunali zilombo zikulu zikulu ziyayima mozungulira mbali mwa dzenje, ndipo anthu amakwera kufuna kutuluka, amakankhidwiranso m'motomo osaloledwa kutuluka. Ndinaganiza, “*Oh, malo ano ndi oopsa, oopsa komanso ozunza.*”

Zinthu zonsezi zikuchitika nthawi imodzi. Ndiwe waludzu, uli ndi njala ndipo watopa. Siumagonanso ku Gahena ayi. Umafuna tulo monga umachitira pano. Thupi lako limafuna kugona. Chibvumbulutso 14:11 amati;

Ndipo utsi wakuzunza kwawo ukwera ku nthawi za nthawi; ndipo sapuma usana ndi usiku iwo akulambira chirombocho ndi fano lache, ndi iye ali yense akalandira lembe la dzina lache.

Sumagona. Tangoganizirani za izi, osagona.

Zokhudzana ndi madzi, mu Zakaliya 9:11,

Iwensu, chifukwa cha mwazi wa pangano lako ndinatulutsa andende m'dzenje m'mene mulibe madzi.”

Kulibiretu madzi ku Gahena.

Ndinadziwa kuti malo a Gahena ali pakati pa dziko. Ndikumene ili, paka pa dziko. Ndinamvetsetsa kuti ndinali mtunda wokwana ma mailosi 3700 kulowa mkati mwa dziko. Tikudziwa kuti chikati kati cha dziko ndi ma mailosi okwana 8000. theka lake lingathe kukhala 4000 mailosi. Ndinali ma mailosi 3700 pansu. Pa Aefeso 4:9 amanena kuti Yesu anatsikira kumalo a pansu pa dziko.

Pa Numeri 16:32 amati,

Ndi dziko linayasama pakamwa pache ndi kuwameza, iwo ndi mabanja awo, ndi amuna awo onse akutsata Kora, ndi akatundu awo onse.”

Kumeneko ndi kumene kuli Gahena tsopano. Kenako Gahena ndi Imfa zizaponyedwa Nyanja ya Moto ndikuponyedwa kumdima wakunja. Izi zizakhala tsiku la chiweruzo litadutsa, koma tsopano ili dziko.

(Ziwanda)

Ndinali mbali mwa dzenje la moto ndipo ndinaona ziwanda zonsezi zitazungulira mbali mwa makoma, masaizi osiyana siyana, maonekedwe osiyana siyana, zooneka zonyansa, mungathe kungoganiza. Zinali zopindika, zopotoka, zikulu zikulu, zing'ono zing'ono. Kunali akangaude akulu akulu, akangaude akulu monga mafiti asanu. Makoswe, njoka ndi mphutsi, chifukwa Baibulo limanena za mphutsizomwe zimakuphimba iwe ([Yesaya 14:11](#)). Kuli mitundu yosiyana siyana ya zinyama zodetsedwa paliponse ndipo zikuoneka zomangidwa komakoma. Ndinadabwa “*Chifukwa chiyani izi zamangidwa kukhoma.*” Sindinamvetsetse izi, koma pali vesi pa zimenezi pa Yuda 1:6 ikuti,

Angelonso amene sanasunga chikhalidwe chawo choyamba, komatu anasiya pokhala pao pawo adawasunga m'ndende zosatha pansu pa mdima, kufikira chiweruzo cha tsiku lalikuru.

Mwina izi ndi zimene ndinaona, sindikudziwa, koma umu ndi mmene zimaonekera. Ndinasangalala chifukwa sindinafune kuti zibwere kwa ine. Zinadana nane ndi mkwiyo wonse! Ichi ndi chinthu china chomwe sindinamvetsetse, sizinali zilombo wamba, zinali ndi mkwiyo pa mtundu wa anthu. Choncho ndinasangalala zinali zitamangidwa kukhoma ndi unyolo.

Ndinayamba kukwera m'dzenjeli kudzera mu mpata wotulukira, ndikuwasiya Malawi a moto. Mosachedwa kunada, koma nditha kuona ziwanda zonsezi mbali mwa makoma ndipo zinali ndi mphamvu zochuluka. Ndinaganiza, “*Ndani amene angamenyane ndi zilombo izi. Panalibe amene akanamenyana nazo izi.*” Koma chonsecho, mantha anali oposa, sindikanatha kupirira mantha amenewa.

(Opanda chiyembekezo)

Chinthu chovuta kwambiri ku Gahena, chovuta kwambiri, chovuta kwambiri koposa kuzunzika, chinali ndinamvetsetsa kuti, poyamba pa zonse, kunali moyo pa dziko lapansi ukupitirira. Ndipo anthu pano padziko, anthu ambiri, alibe maganizo oti dziko ngati ili lilipo pansu pa dziko. Sakudziwa kuti kuli dziko leni leni pansu pa dziko ndipo kuli anthu mabilyoni akuvutika ndipo akupempha mpata umodzi, ngati angathe kutuluka. Koma samapeza mpata otuluka, ndipo amakhala openga paiwo ine kuti sanatenge nthawi yolandira Yesu ndikuti akhala kumeneko mpaka muyaya.

Ichi ndiye chinthu choopsetsetsa chokhudzana ndi Gahena, ndikuti kulibiretu chiyembekezo chotuluka. Ndinamvetsetsa zazimenezi. Ndinamvetsetsa muyaya. Pano pa dziko lapansi, sitingathe kumvetsetsa muyaya. Koma kumeneko ndinamvetsetsa za izi. Ndinadziwa kuti ndizakhala kumeneko mpaka kale kale, ndipo ndinalibe chiyembekezo chotuluka. Ndinaganizira mkazi wanga. Sindingapite kwa mkazi wanga! Ndakhala ndikumamuuza kuti ngati tingazasiyanitsidwe mwa njira ina yake kaya mwa chivomerezi kapena china chake choopsa, ndimati “*Ndizakupeza. Ndizafuna mpaka kukupeza. Ndizakupeza ngati tasiyanitsidwa.*” Koma kuno sindikantha kumupeza. Sindizamuonanso. Sadzadziwa za komwe ine ndili, ndipo sindizayankhula nayenso. Maganizo amenewa amanditsautsa kwambiri! Kusayankhula naye, kusamufikira, ndikusadziwa za komwe ine ndili, ndikukhala opanda chiyembekezo chotuluka! Mukumvetsetsa, sumatuluka kuno, ayi! Taoniani pa dziko lapansi pali chiyembekezo. Ngakhale anthu omwe anali kumalo kozunzidwira amakhala ndi chiyembekezo chotulukako, kapena kufa komabe mwina kutuluka kumene. Koma sitinakumanepo ndi nyengo yopanda chiyembekezo kwathuthu. Pa Yesaya 38:18 akuti,

Pakuti kungsi kwa manda sikungayakuyamikeni inu; imfa singakulemekezeni; Otsikira kudzenje sangaziyembekeze zoonu zanu.

Opanda chiyembekezo, ndipo choonadi ndi Yesu. Ndi choonadi.

(Kuonekera kwa Yesu)

Panthawi imeneyi, ndikukwera pa mpata otulukira, ndipo ndili ndi mantha ochuluka, opanda chiyembekezo, ndikuopa ziwandazi. Mwadzidzidzi, mwadzidzidzi, Yesu anaonekera! “*Ambuye Alemekenzeke*”, Yesu anaonekera. Kuwala uku kuwalitsa malo onse. Ndinangoona maonenekedwe ake, maonenekedwe a munthu. Sindinathe kuona nkhope yake, inali yowala kwambiri. Ndinangoyang’ana kuwala uku ndikuona maonenekedwe ake. Ndinagwada ndikugwa pansi. Sindikanachita chili chonse koma kumulambira. Ndinali oyamika. Kamphindi kamodzi kapitako ndinatayika kwa muyaya, ndipo tsopano mwadzidzidzi ndatuluka kumalo ano, chifukwa ndinali nditamudziwa kale Yesu. Anthu amenewa sangatuluke, koma ndinatha chifukwa ndinali opulumutsidwa kale. Ndinadziwa ndi kumvetsetsa kuti panalibe njira yotulukira malo amenewa, Yesu yekha. Ndi njira yokhayo yokupangitsa kuti usapite kumalo amenewa.

Pa Chibvumbulutso 1:6 akuti, pamene Yohane anapita kumwamba, anaona Yesu, ndi kuti maonenekedwe ake anali owala ngati kuwala kwa dzuwa mu mphamvu yache yonse. Ndipo pamene anamuona Iye, anagwa pansi monga munthu wakufa. Umo ndi mmene ina ndinachitira. Ndinagwa monga munthu wakufa. Tsopano mwina mungathe kuganiza kuti ndinali ndi mafunso mamiliyoni oti ndimufunse, koma ukakhala pamenepo, zonse zomwe iwe ungate kuchita ndikumulambira Iye ndi kutamamnda dzina lake loyera, ndikumuthokoza Iye kuzimene Iye anatipulumutsako ife.

Nditakhazikika, kufika poti ndingathe kuyamba kuganiza, ndinaganiza zoti ndimufunse Ambuye, sindikukhulupirira kuti ndinamufunsa mokuwa, ndinangoganiza ndipo Iye anandiyakha ine. Ndinati, “*Ambuye chifukwa chiyani munanditumiza ine kumalo amenewa?*” “*Chifukwa chiyani munanditumiza ine kuno?*” anati kwa ine “*Chifukwa choti anthu ambiri sakhulupirira kuti malo amenewa alipo.*” Anati “*Ngakhale ena mwa anthu anga sakhulupirira kuti malo awa alipodi.*” Ndinadzidzimuka ndi yankholi. Ndimaganiza kuti Mkhristu wina aliyense akuyenera kukhulupirira za Gahena. Koma si wina aliyense amene amakhulupirira za Gahena yoyaka. Ndinati Ambuye “*Chifukwa chiyani munasankha ine?*” koma sanandiyankhe pa funso limeneli.

Sindikudziwa chifukwa chiyani anandisankha ine kupita kumeneko. Ndine wohepetsetsa kupita kumeneko. Mkazi wanga ndi ine timadana kuonera ma kanema oipa. Timadana ndi kena kali konse koipa. Sindimakondanso ngakhale chilimwe, kutentha pang’ono. Ndi koipa. Kulibe dongosolo. Ndichisokonekero chokha chokha. Ndipo ndimakonda zinthu za dongosolo komanso zolongosoka. Sanandiyankhe pa funso limeneli. Anati kwa ine, “*Pita ukawauze kuti ndimadana ndi malo awa, kuti sichifuniro changa kuti chilengedwe changa chizipita kumalo awa, ngakhale m’modzi! Sindinapangire izi munthu. Ichi chinapangidwira satana ndi a mngelo ake. Uyenera kupita ndipo ukawauze! Ndakupatsa iwe pakamwa, upite ukawauze.*”

Ndinaganiza kwa ine ndekha, “*koma Ambuye, sakandikhulupirira ine. Akaganiza kuti ndapenga kapena ndinagokhala ndi maloto oipa.*” Pamene ndinali kuganiza izi Ambuye anandiyankha ndipo anati, “*Sintchito yako kuti akakhulupirire. Ndi ntchito ya Mzimu Woyera! Ungopita ndikuwauza!*” Ndipo ndinayankha mkati mwanga, “*Inde!*” Ndithudi, ndiyenera kupita ndikukawauza.” Siungadandaule ndikuopa zimene munthu akaganize za iwe, ungapita ndikukachita ndipo Mulungu akachita zotsatirazo. Ameni? Ndipo ndinati, “*Ambuye chifukwa chiyani amandida kwambiri?*” “*Chifukwa chiyani zilombozi izi zimandida?*” Anati, “*Chifukwa unapangidwa mchifaniziro changa, ndipo zimandida ine.*” Ukudziwa satana sangachite kali konse motsutsana ndi Mulungu. Sangamupweteke Mulungu, koma angathe kupweteka chilengedwe chake. Ichi ndi chifukwa chake satana amadana ndi mtundu wa anthu, ndikuwanyenga kuti amutengere ku Gahena. Ndipo amabweretsa nthenda pa iye, china chili chonse chomwe angachite kuononga chilengedwe cha Mulungu.

(Mtendere wa Mulungu)

Kenaka Mulungu anandipangitsa kuti maganizo ake andisefukire. Anandilola kuti mtendere wa mtima wake, ndi m’mene amakondera mtundu wa anthu. Zovuta kuzikhulupirira, ndimakanika kuzimvetsa. Chikondi chimene ali nacho pa munthu, sungathe kuchitenga mnthupi ili. Mukudziwa mmene timakondera akazi athu ndi ana athu? Koteri chikondi chimene tili nacho sitingathe kuchifanizira ndi chikondi chimene Mulungu ali nacho pa ife. Chikondi chake ndi chachikulu koposa chikondi chatu ndikukonda kwathu. Ndichimodzi

modzi monga mmene amanenera pa Aefeso 3:19, “*kuti ndikadziwe chikondi cha Khristu chimene chiposa chidziwitso...*” Chimapitirira kudziwa kwathu, simungathe ngakhale kuchifikira. Sindimatha kukhulupirira za m’mene Iye amakondera mtundu wa anthu, angathe kufera munthu mmodzi kuti asapite kumalo amenewa. Ndipo zimamupweteka kuona mmodzi wa chilengedwe chake chikupita kumalo amenewa. Zimamupweteka Ambuye, Iye amalira kuona munthu mmodzi akupita. Ndipo izi ine zinandikhudza kwambiri.

Ndinaumva mtima wake, anandilola kuti ndikhudze gawo la mtima wake. Anaoneka okhumudwa pachilengedwe chake kupita kumalo amenewa. Ndipo ndinaganiza “*Ndiyenera kupita ndikukachitira umboni ndikugwiritsa ntchito mpweya wanga wonse kupita kukauza dziko lonse za Yesu, mmene ubwino wake uliri.*” Inu, tili ndi uthenga. Ndi nkhani yabwino. Ndikhani yabwino koma dziko silikudziwa. Ayenera kuuzidwa. Mukudziwa tikuyenera kugawana nawo zomwe tikudziwa. Anthu alibe chidziwitso mbali imeneyi. Mulungu akufuna kuti tigawane nawo za ubwino wake, ndi mmene amadanirana ndi malo amenewa.

Anatinso kwa ine, “*Ukawauze kuti ndikubwera posachedwa.*” Ndipo ananenanso, “*Ukawauze ndikubwera posachedwa.*” Tsono tanganzani, chifukwa chiyani sindinanene kwa iye, “*Mukutanthauza chiyani?*” *Kodi posachedwa kwa inu ndi chiyani?*” umu ndi m’mene timaganizira. Koma sindinafunse. Sumanganizanso zofunsa mafunso ngati amenewa nthawi imeneyo. Umangofuna kumulambira Iye kwambiri. Mtendere wa Mulungu umene umabwera pa iwe ikakhala pafupi naye ndiwosafotokozereka. Ndakhalapo mmisonkhano yodzodzedwa, koma simungafanizire ndi chikondi ndi mtendere wa Mulungu omwe mumamva mukakhala pafupi naye.

Kenaka ndinayang’ana ndipo ndinaona ziwanda zija pa khoma, zomwe zinali zoopsa, zimaoneka ngati nyerere pa khoma! Zimangooneka ngati nyerere! Zinali zili zazikulu, koma ndi mphamvu ya Mulungu pafupi naye, mphamvu yonse yolenga, zimaoneka ngati nyerere pa khoma. Sindikanatha kuzidutsa. Ndinaganiza, “*Ambuye zili ngati nyerere!*” Iye anati, “*Ungozimanga ndikuzitulutsa mdzina langa.*” Ndinaganiza “*mphamvu yomwe anapereka ku mpingo.*” Zinthu izi zomwe zinali zoopsa, sitingafanane naye satana popanda Yesu, ayi. Ndizoopsa koma ndi Iye, zili chabe! Kulimba mtima kunabwera pa ine nthawi yomweyo, pamene ndinazona zilombozi ndinamva ngati ndinene kuti, “*inu zilombo ndinu amene mumandizunza ine, kufuna kundikhadzulirana? Bwerani, bwerani tsopano*” ndinayamba mwina kuganiza mwa thupi ndipo ndinaganiza, “*Ambuye zigwireni.*”

(kuchoka ku Gahena)

Pamene timachoka, tinapita kudutsa pa nthaka ya dziko. Tinapita pa mwamba chifukwa tinali tikuyenda mu mphanga yotulukira ija. Posakhalita sindinayionenso, koma zimakhala ngati kamvuluvulu, kamvuluvulu wamkulu yemwe tinalimo. Tinapitabe pamwamba. Timayenera kupita pa mwamba. Pamene tinafika pamwamba pake, ndinayang’ana pansi pa dziko. Dziko limaoneka lokongola. Ndikudziwa Mulungu anandilola ine kuti ndione izi. Anakanatha kuyika njira yotulukirayi m’mene iye akanafunira. Anadziwa zomwe zinali mu mtima mwanga, pamene ndinali wa mng’ono ndimkafuna nditaona mmene dziko limaonekera kuchokera mlenga lenga. Mwina ndinaona nyenyezi zambiri? Ndinangoganiza kuti zinali zabwino kuona dziko, ndikuliona lisakutsamira paliponse. Monga Baibulo limanena. Limati pa Yobu 26:7,

Ayala kumpoto popanda kanthu, Nalenjeka dziko pachabe.

Pamene ukuyang’ana, umaganiza, “*Ndi chiyani chomwe chikugwiriziza ichi? Ndi chiyani chomwe chikupangitsa kuti lizitembuka bwino bwino?*” Mulungu akulodnoleza zimenezi. Mphamvu ya Mulungu yomwe inandikuta ine, inali yodabwitsa. Ali ndi mphamvu yambiri. Chinthu china chili chonse chili pansi pa ulamuliro wake. Palibe tsitsi la mmutu mwanu lomwe limagwa pansi Iye wosadziwa. Palibe mbalame yomwe imagwa pansi iye osazindikira. Ndidzadzidwa ndi maganizo amenewa. Mulungu ali ndi mphamvu yochuluka. Zinandizizwitsa ine. Pali vesi pa Yesaya 40:22 yomwe imati Ambuye amakhala mozungulira dziko. Pamenepo ndinali pozungulira dziko. Ndinaganiza, “*Ambuye, zikutheka bwanji asanabwere*

Christopher Columbus akanatha kuwerenga vesi imeneyi ndikudziwa kuti dziko ndilozungulira.”
Mukudziwa? Anthu amadabwa, amaganiza kuti linali lathyathya?

Chabwino pamene timabwerera tinadutsa zinthu zotchinga; ndinadziwa kuti timadutsa zinthu zotchinga kutentha zomwe zinali mozungulira dziko lapansi. Ndinangodziwa. Ndinaganizanso maganizo opusa, pano ndiri ndi Mulungu, ndipo ndinaganiza, “*Kaya ndiye adutsa bwanji zotchinga zimenezi? Mukudziwa anthu omwe amayenda mlengalenga amayenera kumadutsa moyenera. Tinachidutsa chotchinga popanda vuto liri lonse. Zosadabwitsa! Ndili ndi chikhulupiriro kuti Ambuye amati ndingathe kulongosola zimenezi. Pali vesi pa Masalmo 47:9 imene imati,*

Akuru a anthu asonkhana akhale anthu a Mulungu wa Abrahamu: Akwezeka kwakukuru Iyeyo.

Akulamulira kalikonse, kali konse. Sindinafuno kuti Iye achoke. Ndimangofuna kukhala pamaso pake. Timabwera ku California. Timabwera mwansanga, timayenda mwachangu, ndipo tinafika kunyumba kwathu. Ndipo pamene ndinayang’ana ndimatha kuona kupyoza denga lanyumba. Ndimatha kuziona ndekha nditagona pansu. Izi zinandikhudza kwambiri, chifukwa ndinaliona thupi langa litagona potero ndipo ndinaganiza, “*Uyo sangakhale ine, ndili pano, ine ndine amene ndili pano.*” Mukudziwa inu, simunadzionepo awiri a inu mwini. Ndinali nditagona apa ndipo ndinaganiza, “*Uyo si ine.*” Ndipo vesi ija imene Paulo amanena kuti ife tiri mu msasa (2 Akorinto 5:1) izi zinandikhudza kwambiri. Ndinaganiza “*uwu ndi msasa chabe, ndi chabe. Ndiosakhalitsa. Ine weni weni ndi ine.*” Umu ndi m’mene muyaya uliri. Moyo umene timadandaula nawo, zinandikhudzanso kuti ndife mnthuzi, moyo umenewo ndi mnthuzi chabe monga pa Yakobo 4:14 imakamba mmene moyo umenewo uliri ndi kufupika kwake. Mwachidule. Zaka zana limodzi ngati mungakhale ndi chabe! Zimatha ngati mnthuzi. Ndinaganiza, “*Tikuyenera kukhala moyo wosangalatsa Mulungu.*” Zimene timachita pano, tsopano, zimawerengeredwa kwa muyaya. Tikuyenera kuchitira umboni. Tikuyenera kupita kunja ndikukapulumutsa otaika. Sitingamadandaule ndi zinthu zonsezi zazing’ono zomwe zimatikola kola. Tikuyenera kupita kunja uko ndikukalalikira uthenga ndi nkhani yabwino, chifukwa moyo uwu umatha msanga.

Koma ndinaona thupi langa litagona potero ndipo ndinaganiza zinali ngati wangotuluka mgalimoto yako ndikumaiyang’ana galimotoyo. Imeneyo si iweyo, ndi galimoto yako. Imangokuzungulira. Umu ndi mene ndinazionera ndekha. Thupi langa limangondizungulira pano pa dziko lapansi, koma ine ndiye weniweni. Ndipo ndinaganiza, “*Ambuye musachoke, musachoke*”. Ndimangofuna kukhala ndi inu kanthawi. Koma anachoka. Ndinafika pa mnthupi langa, ndipo china chake chinandikokera kundibwezera mnthupi langa, ngati kuti ndamezedwa mkamwa mwanga.

Pomwepo, pamene anachoka ndipamene mantha onse, kuzunzika konse, kunabwereranso maganizo anga! Chifukwa akunena mbaibulo (1 Yohane 4:18), “*Chikondi chamngwiro chimachotsa mantha.*” Koteri ndinali ndili pafupi ndi chikondi chamngwiro nthawi zonse, tsono chinandichokera, ndipo pamene chinandichokera, mwadzidzidzi mantha onse ndi zoopsa zonse za ku Gahena zinalowa m’maganizo anga. Sindikanatha kupirira! Ndiyamba kukuwa. Ndinali muululu. Sindikanatha kukhala nawo. Ndinadziwa kuti thupi langa silinali lokhonza kupirira kapena kunyamula mantha amenewo. Sungathe kuima pansu pa mphamvu imeneyo. Thupi lanu silamphamvu. Apa ndipamene ndinapemphera ndipo ndinatha kupemphera, “Zichotseni m’maganizo anga!”

Kuthupi, umayenera kudutsa muuphungu wosiyana siyana kuti zinthu zimenezi zichoke koma Mulungu anazichotsa, nthawi yomweyo anazichotsa. Anasiya kukumbukira, koma anachotsa ululu ndi mantha. Ndinali othokoza.

Chabwino, zitatha izi, zinthu zambiri zinachitika, ndikanakonda tikanakhala ndi nthawi kuti ndifotokoze zonse zimene Mulungu anatsimikiza kuti zizachitika kwa ine.

Ngati alipo wina isuku uno, amene samudziwa Ambuye; muyenera kuzifunsa nokha funso. Muyenera kunena, “*Kodi ndikuwakhulupirira anthu awa, kuti zimene anaona ndi zoono, anthu onsewa ndi ine*

ndemwe?” koma makamaka chofunika kwambiri, zimene mau a Mulungu akunena za Gahena. Kondi mukufuna kunena kuti, “*Ayi zindikhulupirira, sindikhulupirira kuti ndi zoono.*” Muyenera kuwataya mau onse kwa Mulungu, ndi ife tonse amene tikuyesesa kukuuzani. Kodi mukufuna kutaya mpata umenewu kunthawi yanu ya muyaya? Izi zingaoneke zopusa kwa ine. Simungalole satana akunyengeni. Chilombo chachikulu chomwe chinali kumapeto, chomwe chimaseka. Umu ndimmene satana amaonekera pamene mwapita ku Gahena. Azaseka, chifukwa munali nawo mpata wolandira Ambuye koma munaphonyana nawo. Koma mukakhala kumeneko, kulibe kubwerera mbuyo. Kulibiretu kubwerera mbuyo. Muzakhala otayika kwamuyaya.

Mungathe kumanena kwa inu nokha. “*Ndine wabwino. Ndine munthu wabwino. Sindikuyenera malo amenewo.*” Ndipo mwina ndinu abwino, kuyerekeza ndi anthu ena. Koma izi sizimene mukuyenera kuziyerekeza nazo. Muyenera kuziyerekeza nokha ndi muyeso wa Mulungu. Muyeso wake ndi wapamwamba koposa wathu. Akunena Mmau ake kuti ngati munama kamodzi, kamodzi kokha moyo wanu wonse, amakupangani inu kukhala wabodza. Ngati munabapo chinthu chimodzi moyo wanu, kapepala, mphindi pang’ono ya abwana ako, kalikonse, kamodzi kokha. Izi zimakupangani kukhala wakuba. Ngati munakwiya opanda chifukwa, ngati simunamukhulukire amene anachita choipa kwa inu. Ngati munakhumbirapo mzimayi, kaya zina mwa zinthu izi, ngati munachita izi ngakhale kamodzi, zimenezi zimakupangani kukhala wochimwa, ndipo simungathe kukwanitsa kupita kumwamba. Choncho onani tonse taperewera. Tapelewera ndipo sitingafikeko ndi ntchito zathu zathu. Tito 3:5 amati,

Zosati zochokera m’ntchito za m’chilungamo, zimene tidachita ife, komatu monga mwa chifundo chache anatipulumutsa ife,

Ameni, zimadalira m’mene mukuziyenera. Zili ngati mzimayi amene anaona gulu lankhosa pa phiri, ndipo zinali zoyera ndi zokongola poyerekeza ndi phiri. Anati, “*Taonani nkhusa zoyera, taonani m’mene zikukongolera, zoyera.*” Anapita kukagona ndipo usiku kunagwa chipale chofewa. Anayang’ana mmawa wake ndipo anaona kuti nkhusa zimaoneka zokuda kuyerekeza ndi chipale chofewa. Kotero tikuyenera kuziyerekeza ndi Mulungu. Muyeso wake ndiwapamwamba koposa wathu. Kotero tikusoweka Mpulumutsi. Sitingapiteko tokha. Mulungu anapanga chipulumutso mphatso yaulere. Anati pa Yohane 14:6, “*Ndine njira, choonadi ndi moyo. Palibe munthu adza kwa Atate koma mwa Ine.*” Ndi njira yokhayo yotulukira malo awa.

Ngati alipo wina amene samudziwa Ambuye, aliyense amene sanamufunsepo Yesu kukhala Mbuye ndi Mpulumutsi wa moyo wanu. Simunafikepo pa malo olankhula ndi pakamwa panu ndi kumfunsa iye kuti alowe mu mtima mwanu, mungathe kuimirira? Ngati alipo wina pano amene angathe kuimirira chifukwa cha Yesu? Musalole satana, chilombo chija chikusekani. Imani tsopano, mpata ukapezeka, chifukwa simudziwa kuti kwakutsalirani nthawi yochulukira bwanji. Simudziwa kuti mutha kufa mawa, ndi kukathera ku malo amenewa.

Ndikuuzeni, malo amenewo, kutentha kokhako ndikoopsa koti munthu ndi kupirira. Anthu amene tinawaona akulumpha pa nyumba zitali zitali za ku New York. Amagwirana manja ndi kulumpha. Zinali zoopsa bwanji. Mukudziwa ngati munakhalapo mwamba ngati m’menemo, ndikuyang’ana pansu, kulumpha kungathe kukhala zosaganizika. Koma amaonyenera kukumana nako kutentha. Ndipo zinali mphindi zochepa unali moto wotentha kwambiri. Ndiye ukuyenera kuupirira kwamuyaya. Ngati muli ofuna kudutsa mudzimenezo, chingathe kukhala chinthu chopusa. Nthawi ndi ino....

(Wotsogolera mwambo kulankhulapo)

Baibulo likumveka bwino bwino, tonse ndife ochimwa, ndipo wina aliyense amene adzaitana pa dzina la Ambuye adzapulumuka. Yesu anati ngati muzandivomereza pamaso pa anthu, inenso ndizakuvomereza pamaso pa Atate wanga wakumwamba. Ndikufuna ndikufunsemi chinthu china. Ngati inu simunalengezepo pagulu pamaso pa aliyense ndi kumvomereza Khristu monga Mbuye ndi Mpulumutsi wanu, kapena ngati

muli osatsimikizika ngati kumwamba kuli nyumba yanu, kumbukirani Yesu anakhomedwa wamaliseche, pa malo amsika, anapachikidwa pamenepo chifukwa cha inu, napirira manyazi.

Ngati mutapemphera pemphero ili kuchokera pansu pa mtima wanu wonse, Mulungu apulumutsa moyo wanu, ndipo akupatsani inu mpata wolowa osati kutsogolo. Pempherani ndi ife, maka maka iwo amene ali mchikhamu ndipo mukudziwa kuti mukuyenera kutero. ***“Mulungu ndikhulupirira mwa inu. Ndinu Wondilenga. Ndine wochimwa. Ndinachimwa malo ambiri, mofuna ndimosadziwa. Ndapelewera. Ndakuphonyani. Ndine wodetsedwa ndi tchimo. Yesu ndikhulupirira mwa Inu. Ndinu mwana wamuyaya wa Mulungu. Ndinu mwana wa Nkhosa wa Mulungu, amene amachotsa machimo awanthu, amene amachotsa machimo anga. Ndikhulupirira munafa pa mtanda. Kukhetsa mwazi wosalakwa chifukwa cha moyo waphulupulu. Ndikhulupirira munaikidwa mmanda ndipo tsiku lachitatu munauka. Ndinu wa moyo kwa nthawi yonse. Ndikutchulani Mpulumutsi wanga. Ndikupatsani moyo wanga. Ndizakukondani, ndizakutumikirani masiku onse amoyo wanga. Ndine wanu, magawo abwino, magawo oipa, magawo auchimo, madongosolo anga, maloto anga, ndikupereka zonse kwa inu. Chifuniro chanu chikwaniritsidwe mwa ine, ndikhulupirira ndapulumsidwa. Osati ndi ntchito zabwino, koma mwachikhulupiriro, pokhulupirira mwa Inu. Mdzina la Yesu ndapemphera. Amenii”.***

Kumvomereza kumeneko ndikofunikira. Baibulo limanena kuti palibe chimwemwe china choposa kuona ochimwa modzi akulapa. Ndipo timangodziwa zitsanzo chochepa cha zimene zimachitika kumwamba kukamaona zimene mwachita lero. Ndikufuna ndilakhule ndi ena a inu, ndipo kenaka ndimaliza nkhanayi. Ndikufuna kuitana iwo amene aona izi. Ndife odala kumva mbale Bill akunena zimene anakumana nazo. Ndikufuna ndikutsimikizireni ndipo ndikufuna kukuchenjezani, musachilandire ichi pokha pokha ngati muli okonzeka kuchita chita mu Uzimu m’ moyo wanu. Sindikufuna kungolakhulapo, ndikufuna kunena kuti musapange kumvomereza uku pokha pokha mukutanthauza izi, ndipo ndichimene ndikufuna kunena. Chili ndi magawo awiri.

Poyamba, sindizaopanso nkhope ya munthu. Chinthu chachikulu chomwe tukuyenera kudziwa kuti kuli kumwamba ndi ku Gahena. Sindizaopa nkhope ya munthu. Kachiwiri, ndizalankhula ndi wina aliyense, masiku onse a moyo wanga zokhuza Yesu, ndi Kumwamba, ndi Gahena. Uku ndi kudzipereka kwathuthu. Munthu wina aliyense ndikumudziwa kuti anafikira anthu za Khristu anafikapo pa fundo ziwiri zakuziperekazi. Chifukwa chiyani kukhala ndi ubale ndi wina aliyense, ngati sikugawana nawo za nkhanu yabwino yomwe imapulumutsa miyoyo yawo ku Gahena. Ndi chinthu chosakhala bwino mu Uzimu kumudziwa munthu wina, kucheza nawo, kusangalatsana nawo, kukhala nawo, ndikulephera kuwauza za Khristu, akupita ku Gahena. Ubale wina uli wonse uyenera ukhale khomo lolumikizirana choonadi chomwe mwachiona lero. Izi ndi zomveka. Ngati simuli okonzeka kuchita izi, ndikumvetsetsa. Koma ngati muli okonzeka kupanga zitsimikizo ziwirizi, ngati mwagwirizana nazo, nenani izi kwa Mulungu, ***“Mulungu ndikukhulupirira mwa inu. Ndikukhulupirira Yesu Mwana wanu, Mzimu wanu Woyera. Ndikulandira chitsimikizo cha ola ili. Ndikulengeza za ine mwini, uku ndi kumvomereza kwanga. sindizaopanso***